

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

CHIPULUMUTSO SICHIZEKA MWA WINA ALIYENSE


MISOZI INAYENDERERA PA NKHOPE PA MNYAMATAYO PAMENE AMADZIKWA-PULA chifukwa cha machimo ake. Kudziko lina, gogo wokalamba, wogwa nkumina, anagwada pansi pa chifano chosema ndipo anapereka ndalama zonse zimene anali nazo. Panthawi yomweyo, kwinanso bambo wachikulire iyeyo asanamwalire anayenda pansi ulendo wautali kupita kumzinda wina umene kwa iye unali wopatulika.

PANTHAWI YOMWEYONSO, mayi wina wachitsikana anagwadira chifano chopatulika, napemphera kuti amuchitire chifundo, nalapa machimo ake kwa wansembe wa chifanocho amene anavala zakuda. Kudziko lina loyandikana nalo, anthu anachita mapemphero mu mzinda wonse pamene miyandamiyanda ya anthuyo inaweramira pansi.

KUDZIKO LINANSO LAKUTALI, bambo ndi mai wina amene anavala zabwino pamodzi ndi ana awo awiri anatenga phala ndi kugawira osauka. Mbali ina ya mseu, anthu awiri amene anali asanakwatirane, anamwa naledzera ndipo anachita zachisembwere pofuna kukwaniritsa zilakolako za matupi awo.

KULIRA KWA NG'OMA kunakulirakulira

pamene mwazi ndi madzi zimathiridwa pa mnyamata wina amene anali wodzidwa ndi ziwanda. Mchipinda china ku dziko linanso lakutali, bambo wina anakhala pansi atapingasa miyendo ndipo anafuna mtendere ndi bata za m'maganizo zimene amazipeza akamalingalira mozama.



KUDZIKO LINANSO LAKUTALI, utsi unaoneka toloo! kuchokera mmudzi wina kumene amapereka nsembe kuti mizimu iwakomere mtima ndipo ichite bata. Kudziko lina lakutali, mtsikana wina anayenda kupita kutsogolo kwa tchalichi kuti akagwirane chanza ndi wolalikira. Ngakhale anthu onsewa akuchokera ku maiko osiyanasiyana ndipo ali ndi zikhulupiriro ndi

zikhulidwe zosiyanasiyana, onsewa ali ndi chinthu chimene chili chofanana. Iwowa akufuna mtendere, kukondwa, kukwaniritsidwa komanso moyo wosatha.

ANTHU AKUYANG'ANA kwa iwo eni, ku ntchito zabwino, ku ntchito zathupi, kwa ansembe, kwa maprofeti, kwa alaliki, ku kupereka nsembe, ku ukaristiya kapena mgonero, ku mpingo, ku zikhulupiriro za mipingo ndi zina zotere. Zonsezi amachita chifukwa akufuna kukwaniritsa chosowa chimene chilipo mu uzimu wao. Iwo amafunafuna chipulumutso ndipo ambiri sadziwa chimene mitima ikufuna kuti akwaniritsidwe.

CHIPULUMUTSO SICHIZEKA mwa wina aliyense kupatula mwa Yesu yekha wopachikidwayo basi.

“Ndipo palibe chipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina

pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo”(Machitidwe 4:12)

ANTHU AKHOZA KUFUNAFUNA dziko lonse napereka nsembe ku zinthu zambiri, koma kufunafuna konseko nkopanda pake pokhapokha ataitanira pa dzina la Yesu Khristu – mwana wa Mulungu wamoyo.

-mws

Chipulumutso Sichizeka mwa Wina Aliyense

Tsamba 1

Ndichite Chiyani Kuti Ndipulumuke?

Tsamba 3

Kusanthula Baibulo—Uchimo

Tsamba 4-5

Mafunso ndi Mayankho: Kodi Mkhristu Angathe Kukhala Moyo Wosachimwa?

Tsamba 6-7

Kodi Mukudziwa/ Mau a pa Nyengo Yake “Pumulani Pakamphindi.”

Tsamba 8

zimene BAIBULO limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chihero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chihero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15



Mau a Mkonzi

Mtima wanga uli wodzaza ndi mayamiko kuti ndinapulumutsidwa ku uchimo kudzera mu mwazi wa Yesu Khristu. Izi sizitengera ubwino uliwonse mwa ine koma ndi chifundo cha Mulungu kuti ndili wopulumutsidwa lero lino. Chinthu chofunikira kuposa kutanthauzira kwabwino kwa Mau komanso chiphunzitso cha Chipulumutso ndi kukhala ndi umboni wakuti munthuwe wapulumutsidwa ndi Mulungu. Zimapereka mtendere wapaderadera kuti pamene ndikukagana usiku kuti ndidziwe kuti machimo anga akhululukidwa ndipo kuti ndine mwana wa Mulungu. Palibe chitsimikizo ngati ichi pamene sindidalira mphamvu zanga, koma za Mpulumutsi wathu amene ali ndi mphamvu za kupulumutsa ndi kusunga. Chokhumba changa ndicho chakuti phunziro la mu kalatayu la chipulumutso ndi uchimo liunikire mitima ndi maganizo athu ku zenizeni zake za nkhanayi komanso kuwonetsa poyera chiphunzitso chabodza pa nkhanayi chimene chakula mdziko lino.

Ndili oyamika kuti kalata uyu akutanthauziridwa mu zinenero za chi Spanish ndi chi Swahili. Tikukhupirira kuti Ambuye atipatsa anthu oti akhoza kumasulira kalatayu mu Chichewa ndi zinenero zina. Ambuye akalola, ndidzapita ku Pakistan kukatumikira pa 23 October – 9 November. Ndisowa mapemphero anu pantchito iliyonse imene ndikuchita polalikira uthenga wabwino. Ndikufuna ndilimbikitse abale anzanga amene tikugwira limodzi ntchito ya uthenga wabwino kuti timenye nkondo yabwino ya chikhulupiriro. Nkhondo ndiye yawirira, koma chigonjetso ndi chathu kudzera mwa Yesu Khristu.

-Michael W. Smith

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawa amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chihero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

CHIPULUMUTSO

KODI NDITANI KUTI NDIPULUMUKE?

Njira Zofunikira Kwambiri

1. MUKHULUPIRIRE – kukhala ndi chikhulupiriro mwa, kapena kuvo-mereza chinthu ngati choona, changwiwo ndi chenicheni.

Machitidwe 16:30-31 nawatulutsira iwo kunja, nati, Ambuye, ndichitenji kuti ndipulumuke? Ndipo iwo anati, Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako.

Yohane 3:16 Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha.

Aroma 10:9 kuti ngati udzavomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu ana-muukitsa kwa akufa, udzapulumuka:

2. MUITANE – kupempha; kufunsira

Aroma 10:13 - pakuti, amene aliyense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.

3. MUVOMEREZE – kunena, kudziwitsa, kulengeza

Aroma 10:10 pakuti ndi mtima munthu akhulupirira kutengapo chilungamo; ndi m'kamwa avomereza kutengapo chipulumutso.

1 Yohane 1:9 Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse.

Miyambo 28:13 Wobisa machimo ake sadzaona mwai; koma waku-wavomereza, nawasiya adzachitidwa chifundo.

4. MULAPE – kutembenuka, kusintha maganizo, kudzimvera chisoni, kukhudzidwa.

Machitidwe 3:19 Chifukwa chake lapani, bwererani kuti afanizidwe machimo anu, kotero kuti zidze nyengo zakutsitsimutsa zo-chokera kunkhope ya Ambuye;

2 Akorinto 7:10 Pakuti chisoni cha kwa Mulungu titembenuzira mti-ma kuchipulumutso, chosamvetsanso chisoni; koma chisoni cha dziko lapansi chichita imfa.

Yesaya 66:2 koma ndidzayang'anira munthu uyu amene ali wau-mphawi, ndi wa mzimu wosweka, nanthunthumira ndi mau anga.

5. MULANDIRE – Kulandira, kulola kuti zikhazikike

Yohane 1:12 Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lake:

Pemphero la Ochimwa

Ambuye Yesu, ndikukhulupirira kuti ndinu mwana wa Mulungu ndipo kuti munafa pa mtanda chifukwa cha machimo anga. Ndikumva chisoni chifukwa cha mphu-lupulu zanga zonse. Ndikhulukikireni ndipo munditsuke ndi mphamvu ya mwazi wanu umene unakhetsedwa. Ndikukulandirani kukhala mpulumutsi wanga ndipo ndikuitanani kuti mulowe mu mtima mwanga. Ndikulapa ndi kusiya moyo wanga wauchimo. Ndikuyamikani chifukwa chomvera pemphero langa ndi kundipulumutsa pokhulupirira dzina lanu. Ndikuyamikani chifukwa cha mphatso ya moyo wosatha. Ndikulemekezani ndi kukulambirani monga Mbuye wa moyo wanga.

-Amen

Zina Zimene Mungachite

I. MUBATIZIDWE - sakramento la kumuviika munthu yense mmadzi ngati chizindikiro cha kutsuka machimo ndi kubadwanso mwa Khristu.

Machitidwe 2:37-38 Lapani Lapani, batizidwani yense wa inu.


Mateyu 28:19 Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.

2. KUBWEZERETSA – kuperekanso kwa mwini wake woyenera chinthu chimene chinatengedwa, kutayika kapena kuperekedwa kwa wina.

Luka 19:8-9 Ndipo Zakeyu anati, “ngati ndalanda kanthu kwa munthu monyenga, ndimbwezera kanai.”

3. KHULULUKIRANI – kupereka chikhulukikiro; kuleka kusunga manga-wa chifukwa cha cholokwa chimene wina anachita, kusiya kupereka chilango chimene chimayenera.

Marko 11:25-26 Ndipo pamene muimirira ndi kupemphera, khululukirani.



Mau a Mulungu:

Aroma 6:13-18

Ndipo musapereke ziwalo zanu kuuchimo, zikhale zida za chosalungama; koma mudzipereke inu nokha kwa Mulungu, monga amoyo atatuluka mwa akufa, ndi ziwalo zanu kwa Mulungu zikhale zida za chilungamo.

Pakuti uchimo sudzachita ufumu pa inu; popeza simuli a lamulo koma a chisomo.

Ndipo chiyani tsono? Tidzachimwa kodi chifukwa sitili a lamulo, koma a chisomo? Msatero ai.

Kodi simudziwa kuti kwa iye amene mudzipereka eni nokha kukhala akapolo ake akumvera iye, mukhalatu akapolo ake a yemweyo mulikumvera iye; kapena a uchimo kulinga kuimfa, kapena a umvero kulinga kuchilungamo?

Koma ayamikidwe Mulungu, kuti ngakhale mudakhala akapolo a uchimo, tsopano mwamvera ndi mtima makhalidwe aja a chiphunzitso chimene munaperekedwera-cho.

Ndipo pamene munamasulidwa kuuchimo, munakhala akapolo a chilungamo.

KALOZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: UCHIMO

1. Chiyambi cha Uchimo

- A. Aroma 5:12 Kudzera mwa munthu mmodzi uchimo unalowa m'dziko lapansi.
- B. Aroma 5:19 Kudzera mu kusamvera kwa munthu mmodzi anthu ochuluka anasanduka ochimwa.

2. Chikhalidwe cha uchimo cha munthu

- A. Genesis 8:21 Lingaliro la mtima wa munthu ndi loipa kuyambira akali mwana.
- B. Aefeso 2:2-3 Mwachibwadwe chake munthu ndi wochimwa.
- C. Aroma 7:14-15 Munthu wosapulumutsidwa ali pansi pa uchimo.
- D. Yereimiya 17:9 Mtima wopanda Mulungu ndi wonyenga ndi woipa ndithu.

3. Kumene uchimo umakhala

- A. Marko 7:20-23 Icho chimene chimadetsa chimachokera mkati.
- B. Mateyu 15:18 Uchimo umachokera mkati mwa mtima.

4. Onse anachimwa

- A. Aroma 3:23 Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemmerero wa Mulungu.
- B. Aroma 3:9 Onse Ayuda ndi Amitundu ali pansi pa uchimo.
- C. 1 Yohane 1:8-10 Tikanena kuti tilibe uchimo, tidzinyenga tokha.

5. Onse amene amachita uchimo ali ana a Mdierekezi

- A. 1 Yohane 3:8a Iye amene amachimwa ali mwana wa mdierekezi.

6. Uchimo umakhudzana ndi kukana dala kuunika

- A. Yohane 15:22-24 Chidziwitso chimaulula za uchimo.
- B. Yohane 9:41 Palibe uchimo pamene palibe kuwala.
- C. Aroma 5:13 Uchimo sukhalapo pamene palibe lamulo.

7. Mayesero sindiwo uchimo

- A. Mateyu 4:1 Yesu anayesedwa ndi mdierekezi.
- B. Ahebri 4:15 Khristu anayesedwa monga mmene timachitira ife, komabe sanachimwe.
- C. Yakobo 1:14-15 Pamene chilakolako chatenga pathupi, chimabala uchimo.

8. Mphamvu ya Uchimo

- A. Aroma 7:14-15 Ndi thupi, palibe mphamvu yogonjetsera uchimo.
- B. Aroma 7:23 Munthu wathupi lanyama amakhala pansi pa ukapolo wa uchimo.

9. Zimene Uchimo umachita

- A. Yesaya 59:2 Uchimo umatilekanitsa ife ndi Mulungu.
- B. Yakobo 1:15 Uchimo umabweretsa imfa.
- C. Yohane 8:34 Uchimo umabweretsa ukapolo.

10. Zotsatira za Uchimo

- A. Yohane 8:21-24 Iwo amene amafa ali mu uchimo sangathe kukhala ndi Khristu.
- B. Aroma 6:23 Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa.
- C. Masalmo 9:17 Oipa adzaponyedwa ku gehena.
- D. Mateyu 25:46 Chilango chamuyaya.
- E. Chivumbulutso 21:8 Kuweruzidwa kuti akaponyedwe mnyanja ya moto.

11. Nsembe za mChipangano Chakale sizikanatha kuchotsa uchimo

- A. Ahebri 8:1-4 Mwazi wa nkhosa ndi mbuzi sunathe kuyeretsa uchimo.
- B. 1 Mafumu 8:46 Nthawi ya chilamulo cha Mose, palibe amakhala osachimwa. (Mlaliki 7:20)
- C. Aroma 8:3 Chilamulo chinali chofooka chifukwa cha thupi.
- D. 1 Akorinto 15:56 Mbola ya imfa ndi uchimo.

12. Kuombedwa kudzera mu chopepesera chochitidwa ndi Khristu

- A. Zekariya 13:1 Nenerani za kuyeretsedwa kwa uchimo.
- B. Mateyu 1:21 Yesu anabadwa kuti akapulumutse athu ake ku machimo awo.
- C. Aroma 5:10-12 Chopepesera uchimo kudzera mwa Khristu.
- D. 1 Yohane 4:10 Yesu ndiye chowombolera cha uchimo wathu.
- E. Ahebri 9:26 Yesu anachotsa uchimo ndi nsembe ya Iye mwini.
- F. 1 Yohane 3:5 Yesu anabwera kudzachotsa machimo athu.

13. Langizo lakuti tisachimwe

- A. Yohane 8:11 Pita, koma usachimwenso. (Yohane 5:14)
- B. Aroma 6:12 Uchimo usachite ufumu m'mthupi lathu.
- C. 1 Akorinto 15:34 Musachimwe.

14. Mphamvu zokhala ndi moyo wopanda uchimo

- A. 2 Akorinto 5:17 Zinthu zakale zapita.
- B. 1 Yohane 5:18 Aliyense amene anabadwa mwa Mulungu sachimwa.
- C. 1 Yohane 1:7 Mwazi wa Yesu umatiyeretsa kutichotsera uchimo wonse.
- D. Yohane 8:36 Inu mudzakhala amfulu ndithu.
- E. Aroma 6:13-18 Uchimo sudzachitanso ufumu.
- F. Tito 2:11-12 Anthu akhoza kukhala moyo wolungama.
- G. 1 Petro 2:21-22 Akhristu ayenera kutsata chitsanzo cha Khristu pa kusachimwa.

MATANTHAUZO A UCHIMO

(CHIPANGANO CHATSOPANO)



1. UCHIMO NDI KUSAWE-
RUZIKA. 1 YOHANE 3:4
2. CHOSALUNGAMA CHI-
LICHONSE NDI UCHIMO.
1 YOHANE 5:17
3. KWA IYE AMENE
AMADZIWA CHABWINO
CHOYENERA KUCHITA,
KOMA OSACHICHITA,
NDIWO UCHIMO.
YAKOBO 4:17
4. CHILICHONSE CHO-
SACHOKERA MU CHI-
KHULUPIRIRO NDI
UCHIMO. AROMA 14:23

Mafunso ndi Mayankho

Funso: Akhristu ambiri amanena kuti aliyense amachimwa “kangapo” pa tsiku lililonse. Kodi mkhristu angathe kukhala osachimwa?

Yankho:

INDE. Akhristu enieni sayenera kuchi-mwa koma ayenera kukhala mmoyo wosachimwa. Izi sizotheka ndi mphamvu kapena nzeru yamunthu. Zimatengera mphamvu ya Mulungu kudzera mwa Yesu kuti munthu akhale m'moyo wosachimwa. Uchimo ndi dzina limene limagwiritsidwa ntchito m'njira zambiri ndipo ndi kofunikira kumvetsetsa kusiyana kwa zolakwika, madera oyenera kukonza komanso uchimo.

ONSE ANACHIMWA

“Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemmero wa Mulungu” Aroma 3:23. Aliyense ndi wochimwa, popeza palibe munthu amene mwa iye yekha angathe kugonjetsa mphamvu ya uchimo. Malamulo a Mose anaperekedwa kuti awulule uchimo kwa anthu. Pa nthawi ya malamulo a Mose, anthu amachimwirabe Mulungu. Ndipo iwo amape-reka nsembe, komabe nsembe zonsezo zinali zosakwanira popeza mwazi wa ng'ombe ndi mbuzi sukanatha kuchotsa uchimo (Ahebri 10:4).

LAMULO LINALI LOSAKWANIRA

“Pakuti chimene chilamulo sichinathe kuchita, popeza chinafooka mwa thupi, Mulungu ana-

tumiza Mwana wake wa Iye yekha m'chifani-
zo cha thupi la uchimo, ndi chifukwa cha
uchimo, natsutsa uchimo m'thupi” (Aroma
8:3). Yesu anabwera ku dziko lino lapansi,
nakhetsa mwazi wake, nafa, ndipo
anaukitsidwa kuti mtundu wa anthu umasu-
lidwe ku mphamvu ndi ulamuliro wa uchimo.
“ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisam-
bitsa kutichotsera uchimo wonse” (I Yo-
hane 1:7). Yesu anabwera “kuti akaononge
ntchito za mdierekezi.” (I Yohane 3:8).

Yesu anawachitira anthu zimene iwo sa-
kanatha kudzychitira paokha pansi pa lamulo.
Anthu akanapitirira kukhala mu uchimo
kudzera mwa Khristu monga zinalili pansi pa
uchimo, mwazi wa Yesu ukanakhalanso
wantchito yanji?



YESU AMAPULUMUTSA KU MPHAMVU YA UCHIMO

Malemba ochuluka amanenetsa kuti ngati
munthu wabadwanso mwatsopano, ndiye
kuti wamasulidwa ndi kupulumutsidwa ku
mphamvu yeniyeni ya uchimo, “pakuti lyeyo
adzapulumsa anthu ake ku machimo
awo” (Mateyu 1:21). “Pakuti uchimo
sudzachita ufumu pa inu; popeza simuli a
lamulo koma a chisomo. Ndipo chiyani
tsono? Tidzachimwa kodi chifukwa sitili a
lamulo, koma a chisomo? Msatero ai”
(Aroma 6:14-15). “Koma ayamikidwe
Mulungu, kuti ngakhale mudakhala akapolo a

uchimo, tsopano mwamvera ndi mtima ma-
khalidwe aja a chiphunzitso chimene
munaperekedweracho; ndipo pamene mu-
namasulidwa kuuchimo, munakhala akapolo a
chilungamo” (Aroma 6:17-18). Nzoonekeratu
kuti pamene munthu amvera Mau a Mulungu
kuchokera mu mtima, iyeyu sangokhululuki-
dwa kokha ku machimo amene anachita ko-
matu amamasulidwa ku mphamvu yeniyeni ya
uchimo. Zenizeni zake za chipulumutso ndiye
kumasulidwa ku uchimo.

“PITA KOMA USAKACHIMWENSO.”

Yesu anamuza mai amene anagwidwa aku-
chita chigololo kuti “pita; kuyambira tsopano
usachimwenso” (Yohane 8:11). Malemba ama-
pitiriza kutiphunzitsa kuti, “Yense wobadwa
kuchokera mwa Mulungu sachita
tchimo...” (I Yohane 3:9). “Chifukwa
chake ngati munthu aliyense ali mwa
Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu
zakale zapita, taonani, zakhala
zatsopano” (2 Akorinto 5:17). Pali kusi-
nthika kodabwitsa kumene kumachitika
pamene munthu wina wapulumutsidwa
kwenikweni kudzera mu mphamvu ya Yesu
Khristu. Mkhristu – amene ali ophunzira
wa Yesu Khristu, angathe kutsata
chitsanzo cha chake cha Khristu ndi ku-
khala moyo wosachita uchimo (I Petro
2:21-22). Anthu ambiri achipembedzo basi
amachipectsa choonadi chooneka ngati
chopusachi nkumanyengezera kuti chime-
nechi sichilungamo.

KODI KUCHITA ZOLAKWIKWA NDI UCHIMO?

Funso limene limafunsidwa ndilo lakuti,
“Mukunena kuti mkhristu sachimwa, ndipo
salakwitsa?” pamenepa ndi pamene pamafu-
nika kumvetsetsa tanthauzo la uchimo.
Mkhristu ali ndi kuthekera kochoka pa
mphamvu ya Khristu ndi kubwerera ku moyo
wa uchimo, komano akatero ndiye kuti sakha-
lanso mkhristu. Pali chisomo ndi mphamvu
zakuti munthu akhoza kukhala moyo
wosachimwa monga mmene akunenera
Malemba.

KUKULA M'CHIKHRISTU

Ngakhale tili akhristu, ndifebe anthu. Nchifu-kwa chake timatha kulakwitsa zinthu ndiponso pena timaperewera mu nzeru. Tili pa ulendo ndipo tikadakula, tifukunabe mphamvu zo-chuluka mu zisomo za Khristu komanso mu chipatso cha Mzimu Wake. Malemba akunena kuti “kulani m'chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu...” (2 Petro 3:18). Mkhristu ali pa ulendo wa kukula mu zinthu za Mulungu – kukula ndi kufanana ndi Khristu. Zidzakhalapo nthawi pa moyo wa mkhristu zimene sadza-khala wopirira kapena wachimwemwe monga mwa nthawi zonse. Akatero sikuti wachimwa koma kuti avomereze chifooko chake ku gawo limeneli ndipo adzikhuthule pamaso pa Ambuye kuti alandire mphamvu ndi chisomo chochuluka.

MTIMA WANGA WAKHAZIKIKA

Mtima wa mkhristu uli ndi chokhumba chimodzi – kukondweretsa Mulungu basi. Mkhristu adzayesedwabe ndithu, monga mmene anachitira Khristu koma osalolera kugonjera ku uchimo (Ahebri 4:1). Kuyesedwa si uchimo monga mmene ena amaphunzitsira. Mkhristu sangathe kuletsa maganizo aliwonse obwera mmutu mwake, koma ali nazo mphamvu zokanika chikhalidwe chauchimo kudzera mu chisomo cha Mulungu.

TCHIMO LIMABWERETSA KULEKANITSI-DWA

Tchimo ndi limene limalekanitsa munthu ndi Mulungu. (Yesaya 59:2). Zinthu zolakwika sizisiyanitsa anthu ndi Mulungu pokhapokha ngati mukunamizira komanso kudzilungamitsa chifukwa cha mtima wodzikuzika. Malamulo a Mulungu okhudza chikhalidwe anaperekedwa kudzera mu Malamulo a Mose. Yesu analimbikitsa chikhalidwe chabwino chimenechi ndipo anaonjezapo muyeso wake popeza iye sanangoyang'ana za tchimolo, koma zimene zili mkati mwa mtima. Izi zikupezeka pa chiphuzitso cha Paphiri (Mateyu 5-7).

MATANTHAUZO A UCHIMO

Chipangano Chatsopano chimapereka matanthauzo anai ofunikira a uchimo – zinthu izo zimene zimatilekanitsa ife ndi Mulungu. “Uchimo ndi kusaweruzika” (I Yohane 3:4). “Chosalungama chilichonse ndi uchimo” (I Yohane 5:17). “Kwa iye amene amadziwa



chabwino choyenera kuchita, koma osachitchita, ndiwo uchimo” (Yakobo 4:17). “Chilichonse chosachokera mu chikhulupiriro ndi uchimo” (Aroma 14:23). Mwana weniweni wa Mulungu sachita mosemphana ndi Malemba amenewa.

MPHAMVU ZOKANIZIRA CHOIPA

Muli mphamvu kudzera mwa Yesu kuti tikhoza kukhala osalakwika malamulo a Mulungu monga mmene zimachitikira panthawi ya Malamulo a Mose pamene anthu amagalukira malamulowo. Mkhristu amene amanena bodza, amaba, amanamizira anzake, amapha, amachita chigololo ndi zina zotere si mkhristunso ameneyo. Kuposera apo, mkhristu weniweni sangakhumbwe ngakhale “kufuna” kuchita zinthu zimenezo. Moyo wosachimwa umachokera ku mtima wachiyero pamaso pa Mulungu. Inde, pakhoza kukhala yesero lofuna kuti munene bodza kapena mube, komatu pali mphamvu imene imapangitsa kuti ganizo lotereli limvere Mulungu. Choncho simuchita kusaweruzika ndipo palibe kuti mwachita kusalongama kapena kuganiza zoipa mu mtima mwanu. Mkhristu amene amadziwa zimene malamulo a Mulungu amafuna ndipo mwadala nasankha kuchita kusamvera, wachimwa ameneyo, chifukwa amadziwa chabwino choyenera kuchita koma sanafune kumvera. Kuonjezera

apo, chimenecho sichinachokere ku chikhulupiriro. Mkhristu ali ndi mphamvu kuti akhoza kukhala molingana ndi chikhulupiriro, mokonda ndi kumvera malamulo onse a Mulungu.

CHIPULUMUTSO CHIMASINTHA ZINTHU

Chipulumutso chimasintha zinthu. Chimangitsa anthu kuti athe kukhala mmoyo wosachimwa chifukwa popeza pali chisomo ndi mphamvu zakuti tikhoza kunena kuti “ayi” kut zinthu izo zimene zingatilekanitse ndi Mulungu. Chipulumutso chimawapangitsa anthu mu umunthu wao kusenderabe chifupi ndi Mulungu ndi kuberekabe chipatso chochuluka cha Mzimu. Zopelewera za anthu si uchimo ayi koma ndi madera chabe akuti tikhoza kukula ndi kuwakonzanso makamaka pamene mtima wathu ukhala woyera ndi wolungama pamaso pa Mulungu.

Chisomo cha Mulungu ndi chokwanira kuti chitigwirizize ndi kutipambanitsa makamaka pakati pa mayeso ndi mayesero a moyo uno. Tiyamika Ambuye chifukwa cha mphamvu zakuti tikhoza kukhala moyo wosachimwa!

-mws



KODI MUKUDZIWA?

MAU AKUTI BAIBULO AKUCHOKERA KU CHIGRIKI AKUTI BIBLIA NDIPO AMATANTHAUZA MABUKU.

BAIBULO NDI NKHOKWE YA MABUKU 66 NDIPO LILI MA CHAPUTALA 1189.

CHIPANGANO CHAKALE CHILI NDI MABUKU 39.

CHIPANGANO CHATSOPANO CHILI NDI MABUKU 27.

MTUMWI PAULO ANALEMBA 14 MWA MABUKU A MU CHIPANGANO

CHATSOPANO.

CHIPANGANO CHAKALE CHINALEMBEDWA MU CHINENERO CHA CHIHEBRI.

CHIPANGANO CHATSOPANO CHINALEMBEDWA MU CHINENERO CHA CHIGRIKI.



Zambiri Zili pa

INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.us

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti muone

makalata akale.



Mau a pa

Nyengo Yake

Mupumule Kamphindi

“Ndipo lye (Yesu) ananena nao, idzani inu nokha padera ku malo achipululu, mupumule kamphindi. Pakuti akudza ndi akuchoka anali piringupiringu, ndipo analibe nthawi yokwanira kudya.” (Marko 6:31).

Yesu ndi ophunzira ake anakangalika kufalitsa Uthenga Wabwino komanso kugwira ntchito yokweza ufumu wa Mulungu. Iwo anali atangomva uthenga wakuti Yohane Mbatizi anali atamudula mutu. Ophunzira aja anagwidwa ndi chisoni, anali wotopa ndi wolema chifukwa ntchito zonse zimene anachita komanso chifukwa cha thukuta limene limadza chifukwa chotopa.

Yesu anawaitana kuti kwa kanthawi achokeko pakati pa chigulu cha anthu ndi ntchito yolemetsa ija kuti apumuleko ndi “Popeza adziwa mapangidwe athu; akumbukira kuti ife ndife fumbi” (Salmo 103:14). Yesu anazindikira kufunikira kodzipatula pakati pa zolemetsa za moyo uno ndi kukhala ndi nthawi yopumula.

Atumiki enieni komanso ogwira ntchito ya uthenga wabwino amanyamula katundu wolemetsa wa miyoyo ya anthu amene awazungulira. Nthawi zina zosowa zathu komanso akatundu amenewa zikhoza kukhala zolemetsa kwambiri. Mbusa wina wachikulire mu mpingo wathu anati, “nthawi zina chazimu kwambiri chimene munthu akhoza kuchita ndicho kupezako katulo.”

Ntchito ya Mulungu ikhoza kukhala yopindula ngati atumiki akhala ndi nthawi yopumula komanso kuusako. Nthawi zambiri atumiki amagwira ntchito kwambiri ndiponso kupanikizidwa chifukwa maitanidwe a Mulungu pa moyo wao komanso kulemera kwa ntchito yakuti igwirike. Atumiki ambiri akhala akudwala matenda oononga mitsempha ndiponso nthenda zina. Nkofunika nthawi zina kuchokapo kaye kwa masiku angapo kapena masabata kupita ku malo ena a phee!, kutali ndi ntchito ya tsiku ndi tsiku, ndi kukapumula komanso kutsitsimuka. Ikhozanso kukhala nthawi yolandira masomphenya atsopano komanso mapenyedwe achilendo pa utumiki ndi kukonzanso bwino ntchito ya Ambuye. Pamene anthu apumula, maganizo awo amakhala omasuka ndipo amatha kuchita zambiri.

Nkofunikira kuti ife tizindikire, monga mmene anachitira Ambuye, kuti tikhale ndi nthawi “yopumulako kamphindi.”



Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.us

CHIYERO KWA AMBUYE

-mws